

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MAUFUMU AWIRI— WAPANSI NDI WAKUMWAMBA

*Pakuti ufulu wathu [boma, ulamuliro] uli
Kumwamba; kuchokera komwenso tilindirira
Mpulumutsi, Ambuye Yesu Khristu—Afilipi 3:20*

Akulu a chikhulupiriro amene afotokozedwa mwatsatanetsatane mu Ahebri 11 anali ochokera ku maiko osiyanasiyana, anakhala mu mibadwo yosiyanasiyana, ndipo anafa imfa zosiyanasiyana; koma anali ndi chinthu chimodzi chofanana. Maso awo anawalitsidwa ndi mapenyedwe auzimu zimene zinawapangitsa kuvomereza kuti iwo anali “alendo ndi ogonera padziko.” Iwowo, pakufuna dziko lakumwamba, cholinga chawo sichinali chakuti ayiwaliretu kapena asaganizireko za dziko lawo la pansi pano.

Nkofunikira kuti ana a Mulungu alero amvetsetse mvemvemve kuti pali maufumu awiri. Ufumu umodzi uli wadziko lino lapansi ndipo winawo ndi ufumu wauzimu. Ufumu umodzi timaulowa pakubadwa mu dziko lino pamene winawo timaulowa “pakubadwanso mwatsopano” kudzera mu Mzimu wa Mulungu (Yohane 3:3). Yesu Khristu ndiye wolamulira ufumu wachiwiriwu pamene anati, “Ufumu wanga sulii wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadambilika nkondo” (Yohane 18:36). Ufumu wa Mulungu uli mwa mwana wa Mulungu aliyense amene anayeretsedwa ndi mwazi (Luka 17:20-21). Si ufumu wa ndale koma ndi ufumu wa “chilungamo, ndi mtendere, ndi chimwemwe mwa Mzimu Woyera” (Aroma 14:17).

Ana ali mzika za dziko limene amabadwiramo. Mwachibadwidwe kuli koyenera kuti anawo akule ndi kuleledwa mwa chikondi komanso kukhala ndi mtima woyamikira dziko lawo. Kukhala nzika ndi chinthu chimodzi chimene chimadziwitsa kuti anthu ali otani komanso

ndilo gawo lalikulu limene limapangitsa kuti munthu amuzindikire mosavuta. Tsoka ilo, anthu amazitengera zinthu pamgong'o pamene akukonda dziko lawo pomwe amalowetsa mzimu wofera ndi kukonda dziko lawo koposa zina zonse. Iwo amalolera kuchita china chilichonse pofuna kuteteza dziko lawo lapansi pano ndipo amalumbira kuti adzipereka ku dziko lawo mpaka ena mwa iwo kufika pokhetsa mwazi.

Mtima wokonda dziko lako nthawi zambiri umatsogozana ndi mzimu wodziwona kuti fuko lanu ndi lapamwamba kuposa ena zimene zili zotsutsana ndi Mzimu wa Mulungu. Izi zili choncho popeza zimene dziko limodzi limakonda zimasiyana kwambiri ndi za dziko lina. Kodi ndi dziko liti kapena anthu ati amene ali opambana pamaso pa Mulungu? Nanga Khristu akanakhala kuti anali pansi pano, akanasankha kukhala nzika ya dziko litilo? Mwa Khristu, “mulibe Myuda, kapena Mgriki” (Agalatiya 3:28) popeza ngakhale kuti pali maiko osiyanasiyana, anthu onse a m'menemo ali ofanana mu ufumu wa Mulungu kudzera mu dongosolo la chipulumutso.

Ngakhale kuti oyera mtima a Mulungu ali nzika za dziko kapena ufumu wa pansi pano, iwo akuitanidwa kuti akhale alendo ndi ogonera pa dziko lino lapansi pamene akufunafuna zinthu zauzimu pamene akukonda ndi kutumikira Mulungu. Ana a Mulungu amavomera maitanidwe opambana ndiponso kudzipereka kwakukulu kosiyana ndi kumene maiko a dziko lino lapansi amakufuna.

Pokhala nzika za ufumu wa dziko lapansi ndi wauzimu, umodzi mwa mafumuwa ukuyenera kukhala patsogolo. Ngakhale kuti kofunikira kwa oyera mtima kuti

(Yapitirira pa tsamba 2)



Ana a Mulungu
amavomera maitanidwe
opambana ndiponso
kudzipereka kwakukulu
kosiyana ndi kumene
maiko a dziko lino
lapansi amakufuna.

Mau a Mkonzi

Kusanthula Baibulo:
Kusabwezera kwa
mkhristu

Nkhani Yotsagana
Nayo:
Kusabwezera kwa
mkhristu

Mafunso ndi
Mayankho
Kutsutsa Mosamala

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

azilemekeza maiko awo ndi kukhala nzika zabwino, zolimbikira ndi zosunga malamulo, iwo akuyenera kuti adzipereke komanso kuonenetsa kuti zikhulupiriro zawo, zikhalidwe zawo ndiponso machitidwe awo ali olingana ndi ufumu wauzimu kusiyana ndi wapansipano. Pamene Yesu amapempherera ophunzira ake mu Yohane 17:14-16, Iye anaonetseratu kuti omutsatira ake, ngakhale anali mu dziko lapansi, komatu sanali a dziko lapansi.

Otsatira a Khristu amakhala ndi zolinga komanso zokhumba zosiyana ndi zomwe maufumu a dziko lino lapansi amaonetsa. Oyera mtima a Mulungu akuyenera kuonetsetsa kuti akudziyang'anira okha poopa kudzipereka kwathunthu zofuna za dziko lawo chifukwa zikhoza kutsutsana ndi zinthu zimene zili zofunikira monga chikondi ndiponso kudzichepetsa zomwe zimafunikira mu ufumu wauzimu. Mzimu wa usilikali kapena mzimu wochita ziwawa sugwirizana ndi Malemba, ngakhale kuti chayambitsa mkanganowo sitikuchidziwa.

Ngakhale kuti oyera mtima padziko lonse lapansi ali ochokera ku

Kwa akhristu, pali malo

a mtendere makamaka

pamene azindikira kuti

ngakhale iwo akukhala mu

ufumu wa dziko lapansi,

komabe unzika wao

ndi chikhalidwe chawo

chenicheni chagona

mu ufumu wauzimu

mitundu, maiko ndi zinenero zosiyanasiyana, umodzi wao upezeka mwa Yesu Khristu. Umodzi umenewo sukuyenera kuwonongeka ndipo oyera mtima sakuyenera kuyambana ndi anzawo chifukwa cha ufumu wa pansi pano. Oyera mtima ali anthu “oitandwa” ndipo akuyenera kukhala m'moyo wachitsanzo.

Mtumwi Paulo, pofanizira ndi nkondo yauzimu anati, “Msilikali sakodwa nazo ntchito

wamba, kuti akakondweretse iye amene adamlemba usilikali.”

(2 Timoteo 2:4). Ana a Mulungu akuyenera kusamalitsa kuti asakodwe mu zochitika za ufumu wa pansi pano. Ndale, kukonda dziko, ziwawa ndi zina zikhoza kuyamba kulamulira moyo wa munthu ndi kumupangitsa kuti asiye kulabadira mfundo za Khristu Yesu zimene zili zozama ndiponso zamuyaya.

Kaya tili mu dziko lotani, nkoyenera kuti tithokoze Mulungu chifukwa cha madalitso ndi zokoma za ufumu wa dziko lapansi zimene tili nazo mu dziko lomwe tikukhalamolo. Ana a Mulungu akuyenera kuyamikira ufulu uliwonse ndi maufulu onse amene akupatsidwa ndi dziko limene anabadwiramo. Komabe kuyamikira kumeneko kusawapangitse iwo kuti ayambe kulonjeza ndikuvomereza zinthu zabodza zimene zimaononga kukhulupirika ndi kudzipereka kwawo kwa mwanawankhosa wa Mulungu. Ngakhale tili alendo ndi ogonera pa dziko pano, cholowa chathu ngati nzika yakumwamba chimaposa kutalitali zimene timazipeza mu maulamuliro a dziko lino lapansi.

Kwa akhristu, pali malo a mtendere makamaka pamene azindikira kuti ngakhale iwo akukhala mu ufumu wa dziko lapansi, komabe unzika wao ndi chikhalidwe chawo chenicheni chagona mu ufumu wauzimu. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutimudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya Gospel Truth imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Zimenenso tilankhula, si ndi mau ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu. —1 Akorinto 2:13

Mutu wathu ulendo uno ndi wa kusabwezera kapena kukonda mtendere. Pali kusiyana ndithu pakati pa matanthauzo awiriwa popeza kukonda mtendere kukhoza kungokhala mtima wokana nkondo kapena boma— zimene zili zosiyana ndi chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano cha kusabwezera. Koma mu kalata uno, kukonda mtendere kukuimira kukana kupita kunkhondo pa zifukwa za chipembedzo.

Chiphunzitso cha kusabwezera chatsamira kwambiri pa Chipangano Chatsopano kusiyana ndi mu Chipangano Chakale. Zimenezi sizikupeputsa zoonadi zake za chiphunzitsochi ngakhale kuti zinthu zambiri zasintha chifukwa cha kubwera kwa Khristu. Nkhani ya kusabwezera ndi mutu kapena zochitika m'moyo zomwe zimafunika munthu wa totomoyo. Ena akhoza kunyoza namanena kuti munthu weniweni amadziteteza pamene wakumana ndi zokhoma, koma zoonadi zake ndi zakuti zimatengera mphamvu ndi nyonga zochuluka kuti munthu ukonde komanso kukhululuka kusiyana ndi kuti ukwinye chibagera kapena ugwiritse ntchito mfuti. Pamene chiphunzitso cha kusabwezera chakhazikika kwambiri pa mfundo yosakoma ya kusapita ku nkondo, chinthu chabwino ndi champhamvu chokhudza moyowu chimene timaphunzirapo ndicho chakuti kusabwezera kukhoza kugwetsa malinga ndi kusintha adani koposa m'mene nkhwangwa kapena chipolopolo chingachitire. Mphamvu ya mtanda ya kusachita nkondo yomwe imapezeka mu khalidwe la kudzipereka kumene kusali kupusa koma kumachokera mu mtima wabwino ndi wachikondi.

Akhristu akhoza kumvetsetsa molakwika za maitanidwe awo pa za kutsatira Yesu mu njira iyi ya kusabwezera koma asanamvetsetse kwenikweni za cholinga cha maufumu awiriwo komanso kuti maufumuwo ali pa nkondo. Ngakhale kuti kubwezera kuli kwake kwa Mulungu mwini yekha, nthawi zina Iye amagwiritsa ntchito maufumu a dziko lino lapansi kuti apereke chiweruzo komanso kukhazikitsa bata ndi mtendere kwa anthu amene ali osasamala za Mulungu. Tikhoza kuchitira ulemu ndi kulemekeza boma limene likutilamulira komanso ufulu umene tili nawo komabe osapereka ulemu umene ukusutsana ndi kudzipereka kwathu komanso kukhulupirika kwathu kumene kumayenera kupita kwa Mulungu yekha. Akhristu ali alendo ndi ogonera padziko pano. Pano tikungodutsa, osadziphatikiza kapena kuyala mphasa mu zochitika za dziko lino. Ndale ndi zina zochitika pakati pathu zimene zimapangitsa kuti mitima ya anthu inyamuke ndi kuiwala za utumiki wao si zinthu zimene zimasonyeza kwenikweni mtima wa Khristu. Padziko pano ndi pa nsasa ndipo tikuyenera kutenga nthawi ndi ntchito yochuluka pokonzekera kwathu kwamuyaya.

Mu zonse zimene timachita, tikuyenera ndithu kudzipereka funso ili kuti, “Kodi Yesu akanachita zimenezi?” Tikuyenera kuyankha funso limeneli posatengera malingaliro kapena zimene zimatisangalatsa, koma potsatira chitsanzo chimene Khristu anatisiyira m'moyo uno. Iye sitimvapo zakuti Yesu amalimbikitsa za ufulu wa ndale pochita nkondo kapena kupanga ziwonetsero m'miseu. Yesu sanamemeze Akhristu kuti apite kukalimbana ndi ulamuliro wa ku Roma kapenanso kuima ndi kudzipereka kwa onse amene amafuna kumuzunza. Iye timawerenga zakuti Khristu anachita koposa m'mene amayembeza, pakuchitira zokoma ndiponso kuwakonda adani ake. Chitsanzo cha Khristu chikuonetsetsa kuti kuchita chipolowe si chinthu chabwino kaya ndiwe mzika yadera kapenanso wotumikira ku boma. Ifeyo ngati mpingo tikuyenera kukwaniritsa kwathunthu udindo wathu aliyense payekhapayekha komanso ngati gulu pofuna kufalitsa uthenga wa mtendere ndi kulola kuti boma ligwire ntchito yake mosalisutsa pochita chiwawa.

John D. Roth anaumba mkota wa izi zonse mu buku lake lotchedwa Choosing Against War, momwe ananena kuti “Pamapeto a zonse, tikamanena za kusachita nkondo kwa Mkhristu si mfundo yakuti tiyambe kukangana mpakana tipambane, kapena chida chongofuna kukwaniritsira zolinga zathu pandale, kapenanso dongosolo linalake la chikhalidwe chabwino. Kumeneku ndiko kudzipereka ku kutsatira Yesu ndi mtima wonse komanso kwathunthu, ngakhale kuti njirayo ititengere mpakana pa mtanda.”

Michael W. Smith

October 2018

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kalozera posanthula Mau a Mulungu

Mutu: Kusabwezera kwa mkhristu

Kuwerenga Malemba: Munamva kuti kunanenedwa, Diso kulipa diso, ndi dzino kulipa dzino: koma ndinena kwa inu, Musakanize munthu woipa; koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lako lamanja, umtembenuzire linanso. Ndipo kwa iye wofuna kupita nawe kumlandu ndi kutenga malaya ako, umlolezenso chofunda chako. Ndipo amene akakukakamiza kumperekeza njira imodzi, upite naye ziwiri. —Mateyu 5:38-41



Mwachidule: Ziphunzitsa ndi zitsanzo za Yesu Khristu zimaonetsera moyo wa chikondi ndi wosafuna chiwawa. Ophunzira ake a Khristu akuitanidwa kuti atsati chitsanzo chake ndipo agwiritse ntchito pemphero, chikondi ndi kukhululuka pamene akumana ndi zoipa kapena chinyengo cha mtundu uliwonse kusiyana ndi kugwiritsa ntchito mphamvu kapena chiwawa. Mpingo wa Mulungu kuyambira mu mbiri yakale ngakhale tsopano umakana kuchita nawo zankhondo.

Matanthauzo: Kusabwezera—Mfundo kapena mchitidwe wosabwezera za chisokonezo kapena ulamuliro wokhazikika umene makamaka pamene ulamulirowo uli wankhanza (dictionary.com).

Kukonda mtendere—Kukana kutenga zida pazifukwa za umunthu kapena za chipembedzo (Merriam-Webster).

I. Uneneri

- A. Yeremiya 31:31 Pangano latsopano (Ahebri 8:13).
- B. Mika 4:2-3 Anthu a Mulungu sadzaphunziranso nkondo.

II. Maufumu awiri

- A. Afilipi 3:20 Ndife nzika za Kumwamba.
- B. Yohane 3:3 Ufumu wa Mulungu timaulowa pakubadwa kuuzimu.
- C. Luka 17:20-21 Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wa uzimu (Aroma 14:17).
- D. Yohane 18:36 Ufumu wa Yesu si wa dziko lino lapansi.
- E. Yohane 17:14-16 Ophunzira a Khristu ali m'dziko lapansi koma osati a dzikolo.
- F. Ahebri 11:13-16 Alendo ndi ogonera m'dziko.
- G. Aefeso 2:19-20 Oyera mtima a banja limodzi.

III. Chiphunzitsa cha Khristu—Lamulo la chikondi

- A. Mateyu 22:36-40 Chikondi ndi lamulo lalikulu koposa (Aroma 13:9-10).
- B. Mateyu 5:38-41 Usakanize choipa. (Luka 6:27-29).
- C. Mateyu 5:43-48 Malangizo a m'mene mungakondere adani anu.

IV. Nkhondo ya oyera mtima

- A. Mateyu 26:51-52 Bweza lupanga m'chimake.
- B. 2 Akorinto 10:3-4 Zida za oyera mtima si za thupi.
- C. Aefeso 6:11-12 Nkhondo yake ndi yauzimu, osati yathupi.

V. Ntchito ya boma

- A. Daniele 2:21 Mulungu amachotsa ndi kukhazikitsa mafumu (Masalmo 75:7).
- B. Daniele 4:17 Wamwambamwambayo alamulira m'maufumu a anthu.
- C. 1 Petro 2:13-14 Atsogoleri a dziko lapansi amaikidwa kuti alange ochita zoipa.
- D. Aroma 13:1-4 Maboma amakhazikitsidwa kuti akwiye onse ochita zoipa (Yeremiya 25:8-9).

VI. Udindo wa oyera mtima

- A. 1 Petro 2:21-24 Kuitanidwa kuti titsati chitsanzo cha Khristu cha kusabwezera.
- B. 1 Petro 3:9 Oyera mtima sakuyenera kubwezera choipa ku choipa.
- C. 1 Petro 2:13-15 Gonjerani maboma ndi maulamuliro a dziko lapansi.
- D. 1 Timoteo 2:1-3 Pemphererani onse amene ali mu maudindo kuti oyera mtima akhale m'moyo odika mtima ndi wamtendere.
- E. 2 Timoteo 2:3-4 Musatangananidwe ndi zochitika za moyo uno.
- F. Aroma 12:14-21 Dalitsani iwo akuzunza inu. Musabwezere inu nokha.

Kumaliza

Pakuti kudzachita ichi mwaitanidwa; pakutinsu Khristu anamva zowawa m'malo mwanu, nakusiyirani chitsanzo kuti mukalondole mapazi ake. —1 Petro 2:21

Kusabwezera kwa mkhristu

KHRISTU AKUTIYITANA KU LAMULO LA CHIKONDI

Yesu Khristu anakhazikitsa chiphunzitso cha chikondi pamene ana a Mulungu amalolera kuzunzika ndi kulandira chilango chosayenera koma iwo osabwezera ndipo amabwezera choipa pakuchita chabwino. Nkhondo ndiponso kukhetsa mwazi zimene zimachitika mu nthawi ya Chipangano Chakale ndi zosalowedwanso kwa anthu a Mulungu pamene tili mu nthawi ya chisomo.

Pangano latsopano

Ngakhale kuti kuchita nkhondo ndiponso chiphunzitso chakuti “diso kulipa diso” zinali mfundo zokhazikika mu mbiri ya fuko la Israele, panali ulosi wakuti padzakhala pangano latsopano. “Taonani masiku adza, ati Yehova, ndipo ndidzapangana pangano latsopano ndi nyumba ya Israele, ndi nyumba ya Israele” (Yeremiya 31:31). Mneneri Mika ananeneratu za nthawi yamtsogolo za anthu a Mulungu kuti “iwo adzasula malupanga ao akhale makasu, ndi mikondo yao ikhale zolimira, mtundu wa anthu sudzasamulira mtundu unzake lupanga, kapena kuphunziranso nkhondo.” (Mika 4:2-3). Maulosi amenewa anakwaniritsidwa kudzera mu dongosolo la chipulumutso la mwa Yesu Khristu.

Lamulo la chikondi

Mu Chipangano Chatsopano, anthu a Mulungu akuitanidwa kuti atsati chiphunzitso ndi chitsanzo cha Yesu Khristu. Mfundo yaikulu ya Khristu inali chiphunzitso cha kukonda Mulungu ndi mtima wako wonse komanso kukonda “mzako monga udzikondera mwini” (Mateyu 22:36-40). Ana a Mulungu akuyenera kukhala ndi chikondi chachikulu komanso chisamaliro cha pa anthu onse ndi kufunira zabwino anthu onse, ngakhale ochita zoipa. Pamene Aisraele, anali kuchita zankhondo, ali pansi pa chitsogozo cha Mulungu, Yesu anaphunzitsa kulekela ndi kusabwezera. “Munamva kuti kunanenedwa, Diso kulipa diso, ndi dzino kulipa dzino: koma ndinena kwa inu, Musakanize munthu woipa; koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lako lamanja, umtembenuzire linanso.” (Mateyu 5:38-39). Ndimayi imapereka malangizo pamene munthu wayambana ndi mnzake, komanso kwa anthu a mtundu wa Chiyuda amene anali kukhala pansi pa ulamuliro wankhanza wa boma la Aroma. Ngakhale kuti anthu ambiri amadikirira Mesiya amene adzawatsogolere kunkhondo yolimbana ndi Aroma, m'malo mwake Mesiyo analalikirira zakuti “musakanize munthu woipa.”

Chitsanzo cha Yesu

Kodi Yesu ankanenadi zenizeni pamene amati anthu ake asachite kapena kupita ku nkhondo? Mau akewo anali oposa nkhabakamba kapena kulankhula mwa njerengo. Inali nthawi yofunikira kwambiri pamene Yesu anatsala

pang'ono kuti aphedwe, Iye analamulira Petro kuti abweze lupanga lake m'chimake. (Mateyu 26:52). M'malo mogwiritsa ntchito mphamvu kapena chipolowe polimbana ndi zoipa komanso kusalungama, Yesu anazunzika popanda kuopseza kapena kubwezera. Iye anapemphera kwa Atate kuti awakhululukire adani ake. Yesu, anachitira umboni ndi moyo wake womwe, monganso anachitira omutsanzira ake, kuti kulandira mazunzo ndi chisalungamo mwachikondi kuli kwabwino kusiyana ndi kubwezera kapena kuchita nkhondo pawekha ngati munthu kapenanso m'dzina la boma.

Kuli koyenera kwa ana oona a Atate kuti asiye zinthu zonse zimene zimayambitsa nkhondo kapena chiwawa. “Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako: koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; koterokuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba” (Mateyu 5:43-45).

Nkhondo yauzimu

Paulo, ponena za nkhondo yauzimu, analengeza momveka bwino kuti “Pakuti pakuyendayenda m'thupi, sitichita nkhondo monga mwa thupi, (pakuti zida za nkhondo yathu sizili za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga)” (2 Akorinto 10:3-4). Zida za nkhondo yathuzo sikutu zili za thupi ayi, koma ngakhale mzimu wa nkhondowo uli wosutsana ndi mzimu wa chikondi. Yesu anati, “pakuti onse akugwira lupanga adzaonongeka ndi lupanga” (Mateyu 26:52). Moyo wa Mkhristu udzikhala woperekedwa ku ntchito ya Khristu ndiponso ku uthenga wa mtendere. Pamene oyera mtima ali pa mikangano ndi nkhondo, nkhondoyo idzikhala yauzimu osati yathupi. “kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi” (Aefeso 6:11-12).

Umboni wochokera mu mbiri

Malingana ndi zolembedwa za mu mbiri yakale, akhristu oyamba anakaniratu nkhondo komanso kukhetsa mwazi potsata chiphunzitso cha Khristu. Akatswiri a mbiri yakale amati, nthawi zina kunena mwatchutchutchu kuti kusabwezera ndiyo mfundo imene akhristu

(Yapitirira pa tsamba 6)



“Inali nthawi
yofunikira
kwambiri
pamene Yesu
anatsala
pang'ono kuti
aphedwe, Iye
analamulira
Petro kuti
abweze lupanga
lake m'chimake.”

(Kuchokera pa tsamba 5)

anatsamirapo kuyambira pachiyambi. Akhristu a mpingo woyamba anakana kutumikira ku nkondo chifukwa cha chikhulupiriro chawo ndi kumvera Khristu. Mzaka za pakati pa 100-200 AD, munthu wina wotchedwa Justin Martyr analemba kuti: “ife...tasintha...zida zathu zokhala ngati zankhondo, malupanga athu kuwasandutsa makasu,

ndipo mikondo yathu kukhala zipangizo zolimira.” Malamulo a mpingo woyamba amakaniza kutumikira kunkhondo.



“Pali kusiyana kwakukulu

pakati pa zofuna za

ana a Mulungu amene

akukhala pansu pa

chisomo ndiponso

udindo umene Mulungu

waika pa maulamuliro

a dziko lapansi amene

akulamulira mwathupi.”

Maboma a “Chikhristu” anadzetsa moyo wotayirira

Pali umboni wokwanira kuchokera mu mbiri ya mpingo kuti mipingo inayamba moyo wolekerera pa nthawi imene akhristu anayamba kupita nawo ku nkondo. Poyankhapo pa nkhanayi, mmodzi mwa akuluakulu a mpingo woyamba dzina lake Tertullian analemba m’chaka cha A.D. 174 kuti, “Kodi mwana wa mtendere adzatenga nawo gawo mu nkondo pamene iye sangathe kutsutsa lamulo lake?” Tertullian anapitiriza kulemba nati ngati msilikali watembenuka mtima, nthawi yomweyo iye asiye usilikaliwo ndipo alolere kulandira chilango chimene

chingaperekedwe chifukwa cha zimene wachitazo.

Pamene mfumu yaikulu ya chiroma dzina lake Constantine inatembenuka mtima m’chaka cha 312 A.D., inalamula kuti chikhristu chikhale chovomerezeka mwa lamulo. Zimenezi zinapangitsa kuti akhristu ayambe kusintha pa mchitidwe wao wa kusabwezera, popeza tsopano ulamuliro wa nthawiyo sikuti unalinso wachikunja. M’chaka cha 380 A.D., mafumu achiroma aakulu amene amalamulira maina awo Theodosius ndi Gratianus anapangitsa chikhristu kuti chikhale chipembedzo cha dziko ndipo zotsatira zake asilikali onse amayenera kukhala akhristu. Ichi chinakhala ngati chabweza pambuyo nkhanu ya kusabwezera imene chikhristu choyambirira chinatsamirapo ndipo amene analimbikitsa mfundoyi anali atsogoleri ankondo amene amamenya nkondo akudzitchula kuti ali akhristu.

Kusiyantsa pakati pa zadziko ndi zauzimu

Akhristu ambiri masiku ano nawonso atayirira pa zimene anakhazikikapo zokhudza nkhanayi. Mwana wa Mulungu akuyenera kukhazikika pa mfundo ya chiphunzitso cha Khristu ya kusabwezera osati pa zimene zikupezeka mu mbiri ya mpingo. Nkofunikira kwambiri kuzindikira maufumu awiriwa—umodzi ndi wakanthawi ndipo winawo ndi wauzimu. Ufumu wa Mulungu “suli wa dziko lino lapansi” (Yohane 18:36) ndipo Akhristu, ngakhale ali a dziko lapansi, sali a dzikolo (Yohane 17:14-16). Pokhala ogonera ndi alendo, oyera mtima a mu Ufumu wa Mulungu akuyenera kukana nkondo yobwera chifukwa cha boma kwa kanthawi kocheba chifukwa chakuti ikutsutsana ndi zimene mzika ya ufumu wa uzimu imayenera kuchita. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa

zofuna za ana a Mulungu amene akukhala pansu pa chisomo ndiponso udindo umene Mulungu waika pa maulamuliro a dziko lapansi amene akulamulira mwathupi. Nthawi zambiri ziwirizi zimadalirana ngakhale chilichonse chimaoneka kuti chili pachokha.

Maulamuliro ndi okhazikitsidwa ndi Mulungu

Buku la Daniele likutiphunzitsa kuti Mulungu ndiye amene “achotsa mafumu, nalonga mafumu” (2:21). “Wam’mwambamwamba alamulira m’ufumu wa anthu, naupereka kwa aliyense Iye afuna, nauutsira wolubukira anthu.” (4:17). Ngakhale kuti maulamuliro a pansu pano sangakwanitse mwa malamulo awo kubweretsa chimango ndi mtendere wathunthu chifukwa chakuti anthu amakana chisomo cha Mulungu, iwowo akhoza kuyesera kuchepetsako chipolowe pogwiritsa ntchito njira za kuthupi. Nchifukwa chake, Mulungu anaika kuti mafumu ndi a bwanankubwa adzilanga onse ochita zoipa. (1 Petro 2:13-14). Si ntchito ya anthu oyera mtima okhala mwa chikondi ndi chisomo kuti adzipereka chilango kwa iwo amene akuchita nkhanza kapena kwa zigawenga kapenanso dziko lopulupudza. Olamulira a dziko lino, amene akutchedwanso kuti “atumiki a Mulungu”, anaikidwa ndi Mulungu kuti “akwiyire ndi kubwezera chilango wochita zoipa” (Aroma 13:1-4).

Maitanidwe a Mkhristu

Cholinga chenicheni cha mpingo ndicho kukhala nthambi yopititsa patsogolo cholinga chachikulu cha Khristu pa dziko lino lapansi. Udindo wa Khristu sunali kulanga wochita zoipa koma kubweretsa uthenga wa chipulumutso ndi chikondi kudziko lino lochimwali. Pokhala mzika za dzikoli, ntchito ya Mkhristu ndiko kukhala monga mwa maitanidwe opambana. Baibulo limanena za ntchito ndi udindo wa mwana wa Mulungu. “Tadzigonjani kwa zoikika zonse za anthu, chifukwa cha Ambuye” (1 Petro 2:13). Akhristu akuyenera kumvera malamulo a dziko lawo pokhapokha ngati malamulowo sasutsana ndi malamulo a Mulungu. Akhristu akuyenera kupemphera ndi kupembedzera “chifukwa cha mafumu ndi onse akuchita ulamuliro; kuti m’moyo mwathu tikakhale odika mtima ndi achete m’kulemekeza Mulungu, ndi m’kulemekezeka monse. Pakuti ichi nchokoma ndi cholandirika pamaso pa Mulungu Mpulumutsi wathu” (1 Timoteo 2:1-3). Cholinga chake ndicho chakuti tikhale m’moyo wachete ndi wamtendere; ndipo pokhala asilikali a mtandawo, akhristu sakuyenera kudzitanganidwitsa ndi zochitikachitika za moyo uno (2 Timoteo 2:3-4).

Pamene nkondo zikumenyedwa ndipo maiko amauka ena ndikugwa, oyera mtima a Mulungu akuyenera kupitirirabe kutsatira mapazi a Khristu (1 Petro 2:21-24)—“osabwezera choipa ndi choipa” (1 Petro 3:9), okhala ndi chikondi chosanyenga, ochitira zabwino adani athu ndi a dziko lathu, odalitsa iwo akutizunza, ndipo ogonjetsa choipa pakuchita chabwino (Aroma 12:14-21).

Oyera mtima amakhazikika pa mfundo yakuti sakuyenera kuchita nkondo potsatira chiphunzitso ndi chitsanzo cha kalonga wa mtendere. Dziko lapansi silidzachimvetsetsa chiphunzitso cha kusabwezera ndipo chidzabweretsa masautso, mwinanso imfa kumene, koma chili gawo limodzi la njira yophaphatiza imene imatitsogolera ku moyo wosatha. ■

Mafunso

?

Mayankho

Kodi ndi kolakwika kwa Mkhristu kuchita nkondo pofuna kudziteteza?

Funso limeneli limabweretsa mayankho komanso makangano amene angapangitse kuti mitima ya anthu inyamuke. Nkofunikira kudziwa kuti akhristu (molakwika) anabweretsa “mfundo ya nkondo yovemerekeza” pofuna kuti nkhani ya nkondo ilumikizane ndi chiphunzitso cha kusabwezera. Zoterezinso zikhoza kuchitika pa pamene munthu akufuna kudziyikira kumbuyo. Khristu sanadziteteza pamene anatengedwa kuti akamenyedwe ndi kupachikidwa pamtanda. Atumwi ndiponso zikwizikwi za anthu amene anaphedwa chifukwa cha Khristu nawonso sanabwezere kapena kulimbikira kudziteteza pamene anawaweruza mwachipongwe kuti akaphedwe. Nzosamveka kuti munthu akhoza kusadziteteza pamene waopsezedwa, nchifukwa chake zimafunikira chisomo chochokera kumwamba ndi kuthekera

kuchokera kwa Mulungu kuti munthu ubwezere ndi mphamvu yaikulu ya chikondi komanso kukhululuka.

Panali nthawi zambiri pamene chikhamu cha anthu chinafunitsitsa chitamugwira Yesu ndi kumupha. Yesu anawathawa ndipo anawazemba koposa kangapo konse. Nchifukwa chake, kumuthawa munthu wochita zolakwitsa kukusiyana ndi kudziteteza. Pali nyengo zambiri zimene tingathe kuzinena ngati kuti zimaoneka ngati zikutsutsana ndi choonadi chimenechi. Ineyo ndikuvomereza kuti mwakufuna kwanga ndichita zonse zotheka kuti ndiwauze ana kuti asamachite nkondo pofuna kupulumuka kwa munthu amene wawagwira mowakakamiza. Mulungu walonjeza kuti sadzaika pa ife mtolo woposa m'mene ifeyo tingakwanitse kuwusenza, ndipo ndikukhulupirira kuti mu nyengo zovutitsitsa pamakhalanso chisomo ndi nzeru zoposetsa kuchokera kwa Muungu kuti tikwanitse kusunga chiyero chathu chauzimu.

Kodi Mkhristu angachite chiyani pofuna kuthandiza iwo amene amagwira ntchito yosungitsa bata komanso ya usilikali?

Pokhala nzika zabwino za chikhristu, sikuti tikuchita za chiphamaso pamene tiyamikira udindo ndi ntchito zokhazikitsa bata komanso za usilikali zimene dziko limachita ngakale kuti ifeyo sititenga nawo gawo mu zochitika zimene zikhoza kuchotsa moyo wa munthu wina. Popanda asilikali okhazikitsa mtendere m'dziko mwao kapenanso kunja kwa dziko lawo, kukanakhala chisawawa chokhachokha ndipo ufulu ukanachepa. Timakhala pa ufulu chifukwa cha kudzipereka kwathunthu kwa anthu amene amalolera kuika moyo wao pachiswe kuti ifeyo tikhale pabwino. Pali ntchito zina zothandiza komanso zauzimu zimene akhristu angachite kwa iwo amene akugwira ntchito yosungitsa bata komanso ya asilikali ankondo. Nkofunika kukumbukira kuti akhristu ali nzika za maiko awiri. Utumiki wathu ndi mfundo zoyendetsera moyo wathu zazikika pa zauzimu, komabe zimenezi sizitiletsa ife kuti tisayamikire zimene asilikali athu amachita.

Nkofunikiranso kuti akhristu asakometsere ntchito ya boma ngakhale kuti bomalo limagwira ntchito yofunikira kwambiri kwa iwo amene sakhalanso pa chisomo. Chimakhala chinthu cholakwika kwa ana athu pamene tilimbikitsa maitanidwe komanso ntchito zimene sizigwirizana ndi chikhalidwe cha chikhristu.

KUTSUTSA MOSAMALA

Kumvera Mulungu kusiyana ndi kumvera munthu

Munthu wotsutsa mosamala ndi iye amene amakana kutumikira ntchito ya usilikali kapena kupita kunkhondo chifukwa cha zolinga za umunthu kapena zachipembedzo. Kuyambira kale ndithu, mbiri imationetsa kuti anthu otsutsa mosamalawa amamangidwa kapena kunyongedwa kumene pamene zikhulupiriro zawo zitsutsana ndi za dziko lawolo.

Ena otsutsa mosamala amalolera kugwira ntchito pakati pa asilikali koma ntchito zake zosakhudzana ndi nkondo, pamene ena amakaniratu kugwira ntchito iliyonse yokhudzana ndi za asilikali ankondo. Mu nthawi za masiku ano, maiko ena amaikiratu kapena kuperekeratu mpata wakuti munthu akhoza kukhala otsutsa mosamala pazifukwa za chipembedzo. Ena mwa maiko amenewa amapereka ntchito zina zimene munthuyo akhoza kuzigwira m'malo mopita kunkhondo. Ntchito zake zimakhala za mu ofesi pofuna kuti zilowe m'malo mwakuti munthuyo akadakhala msilikali.

Akhristu akuyenera kuyesetsa kuti achite m'mene angathere kuti agwire ntchito motsatira zimene malamulo a dziko lawo amafuna pofuna kukhala nzika yaphindu monga m'mene limafunira lamulo. Koma pamene zoterezi zifika potsutsana ndi chifuniro cha Khristu, modzichepetsa mkhristuyo akuyenera kumvera lamulo la Mulungu kusiyana ndi kumvera lamulo la munthu. ■





KODI MUKUDZIWA?

Usaphe. —Eksodo 20:13

Mamasulidwe ena a baibulo amagwiritsa mau akuti “kupha,” koma liwu labwino kuligwiritsa ntchito pomasulira mu ndimeyi ndilo “kupha mwa umbanda”. Kupha mwa umbanda pamene munthu watenga moyo wa munthu wina mophwanya lamulo komanso mwadala makamaka chifukwa cha kaduka.

Sipanapite nthawi kuchokera pamene lamuloli linaperekedwa, kuti Mulungu analamulira Alevi kutenga lupanga ndi kupha munthu wina aliyense amene anatembenukira ku mafano. Mulungu samachita zosutsana ndi lamulo limene anapereka kwa Mose, popeza kuphako kunali kwakuti kukwaniritse chilungamo.

Ngakhale kuti baibulo limaikapo mtima kwambiri pa kufunikira kwa moyo wa munthu, lamulo ili makamaka si maziko a kuzabwezera choipa kumene tikupeza mu Chipangano Chatsopano.



**Mau a pa
Nyengo
Yake**

CHOONETSEDWA KU DZIKO LAPANSI


Pakuti ndiyesa, kuti Mulungu anaoneketsa ife atumwi otsiriza, monga titi tife; pakuti takhala ife choonetsedwa kudziko lapansi, ndi kwa angelo, ndi kwa anthu. Tili opusa ife chifukwa cha Khristu.... —1 Akorinto 4:9-13

Mtumwi Paulo akupereka chithunzi chenicheni cha masautso ndi mazunzo amene atumwi anakumana nawo mu 1 Akorinto 4:9-13. Chimenechi ndi chilimbikitso komanso chobetchera kwa atumiki a uthenga wabwino amene akugwira ntchito modzipereka.

Paulo akunena za mchitidwe umene umachitika pakati pa Aroma m'nthawi imeneyi pamene iwo amabweretsa anthu atavala zodzitetezera, komanso atanyamula zida, ndi kuwalowetsa mu bwalo la masewero kuti amenyanane ndi zilombo zakuthengo. Munthuyo akapuluma, amalanda zida zake ndi zodzitetezera zija kuti chilombo chija chimupwetedze. Ngati apulumukanso pamenepa, amaumirizidwa kuti alimbane ndi munthu wina wachiwiri woala zodziteza ali ndi zida mpaka woyambayo atafa. Atumiki a uthenga wabwino akhoza kukumana ndi mayesero, mazunzo, kunamiziridwa, umphawi ndipo masautso ochuluka m'moyo uno; koma chili chinthu chaulemu kuti iwowo ayesedwe oyenera kuzunzidwa chifukwa cha dzina la Khristu.

Nthawi zambiri anthu a Mulungu amakhala ngati “choonetsedwa kudziko lapansi.” Choonetsedwacho chikukamba kwenikweni za bwalo lochitira masewero kumene anthu amachita masewero ofanana ndi nkonya. Bwalolo limakhala ndi malo akuti anthu miyandamiyanda akhoza kukhala ndi kumaonerera omenyanawo mpaka mmodzi wa iwo atafa kapena kuonerera chigawenga china chikhuphedwa chifukwa cholakwira lamulo. Oyera mtima a Mulungu azunguliridwa ndi dziko lapansi. Nthawi zambiri anthu oyera amanyozedwa ndi kunenedwa popeza amaonedwa ngati anthu osalungama. Mfundo zazikulu zoyendetsera mtima ndi moyo wa mwana wa Mulungu zili zosiyana kwambiri ndi za dziko lapansi. Dziko silimvetsetsa ndipo nthawi zambiri limanyoza ndi kumusala mwana wa Mulungu. Oyera mtima a Mulungu akuyenera kuyang'ana ndi kuchita zinthu mosiyana ndi dziko lapansi. Iwo amakonda ndiponso kukhululuka osati kubwezera kapena kuchita nkondo. Iwo amalalikirira za kudzichepetsa, chikondi ndi umodzi kusiyana ndi kulalikirira za kungosamalira zathupi za iwo wokha komanso kudzikuzi. Nzosadabwitsa kuti oyera mtima a Mulungu ali ngati choonetsedwa.

Mdaniyo akuyesetsa kuchita nkondo kuti afooketse ndiponso kugwetsa mphwayi atumiki amene akukangalira pa utumiki. M'malo mofooka kapena kukhumudwa chifukwa cha zokhoma zimene tikumana nazo m'moyo uno, tiyenera tilimbe mtima! Sitikuyenera kuchita manyazi chifukwa chakuti taima njii komanso mokhulupirika pa Mau a Mulungu ndipo tikulalikirira uthenga wopereka moyo wa chipulumutso ndi chiyeero. Monga momwe ena anazunzika chifukwa cha Khristu, nafenso tidzatero. Khalani okhulupirika, popeza ndife mafumu ndiponso ansembe mu ufumu wa Ambuye wathu. ■



Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE